mudzanene. Lalikirani ulaliki ngati inu mungathe. Bweretsani pepala lanu ku kalasi.

===========================================================================

17. Kodi chimachitika ndi chiyani ngati titumikira Mulungu ndi zinthu za dziko lapansi? ______________________________

______________________________

Lembani Mateyu 6:33: ______________________________

______________________________

______________________________

===========================================================================

1. Yesu anati ndi kofunika kusankha moyo wosakonda chuma.

Kodi chidzaoneka ndi chiyani ngati ife titayesa kutumikira Mulungu ndi zinthu za dziko lapansi? ______________________________

______________________________

Mateyu 6:33: ______________________________

______________________________

______________________________

==========================================================================

2. Ngati ife tiyesa kutumikira Mulungu ndi chuma, tikhoza kudana ndi wina ndi kukonda winayo. Tsopano pezani Mateyu 6:33 m'Buku Lopatulika. Onani ngati mwalemba bwino. Siyani Buku Lopatulika lili chitsegulire.

Lero tiyeni tipitirize ndi chiphunzitso cha Yesu cha pa phiri. Apanso Yesu anaphunzitsa za njira imene tingakhalire ndi anzathu. Ndipo Iye anaphunzitsa zina zambiri za Mulungu. Chimenechi ndi chimene tiphunzire lero.

(1) Pamene tikuganiza zoweruza ena poyamba tiyenera kudziyang'ana tokha.

(2) Mateyu 7 amaonetsa kuti m'njira yomwe ife timapatsa zinthu kwa ana athu Mulungu adzatipatsanso ife zinthu zabwino pamene tipemphera.

Tsopano tengani Buku Lopatulika ndi kuwerenga Mateyu 7:1 mpaka 11. Werengani ndime 1. Kuchokera m'ndime imeneyi, kodi tiyenera kuweruza ena?

______________________________

==========================================================================

3. Yesu amati sitiyenera kuweruza ena. Pali zifukwa zake za zimenezi.

Mateyu 7:1-2:

Musaweruze, kuti mungaweruzidwe. Pakuti ndi kuweruza kumene muweruza nako inunso mudzaweruzidwa; ndipo ndi muyeso umene muyesa nawo, kudzayesedwa kwa inunso.

Kodi chimaoneka ndi chiyani ngati tiweruza ena?

______________________________________________

==================================================================

4. Ngati ife tiweruza ena, ifenso tidzaweruzidwa. Tidzaweruzidwa mwa njira yomwe ife tiweruzira enayo. Pamene tikuyang'ana kwa anthu ena, timaona zolakwa zawo. Timaiwala kuti ifenso tiri ndi zolakwa. Zinthu zimene anthu ena amachita zimativuta ife. Timaganiza kuti iwo ayenera kusintha. Nthaŵi zina timaganiza kuti ife ndife angwiro ndi kuti sitingalakwe.

Mateyu 7:3:

Ndipo upenya bwanji kachitsotso kali m'diso la mbale wako, koma mtanda uli m'diso la iwe mwini suunganizira?

Kodi inu nthaŵi zina mumafuna kumaweruza anthu ena? ______________

==================================================================

5. Nthaŵi zina ife timafuna kumaweruza anthu ena. Ndi chinthu chapafupi kuona zolakwa zawo. Timafuna kuwauza iwo pamene alakwa. Ife timafuna kuŵauza iwo zomwe angachite. Koma njira imeneyi sinjira yakayambidwe kabwino.

Mateyu 7:4:

Kapena udzati bwanji kwa mbale wako, 'Tandilola ndichotse kachitsotso m'diso lako; ndipo ona, mtandawo ulimo m'diso lakoli.

Kodi ndi zolakwa za yani zomwe tiyenera kuziona poyamba ndi zolakwa zathu kapena zolakwa za anthu ena?

______________________________

==================================================================

6. Poyamba tiyenera kuona pa zolakwa za ife eni. Ngati nthaŵi zonse titamachita zimenezi, zidzatithandiza ife kwambiri. Zidzathandiza mpi-

ngo kuti ukhalire pamodzi mwa mtendere.

Mateyu 7:5:

> Wonyenga iwe! tayamba kuchotsa m'diso lako mtandawo, pomwepo udzapenyetsa kuchotsa kachitsotso m'diso la mbale wako.

Kuchokera m'ndime imeneyi, kodi ndi liti kwenikweni lili labwino kudziyang'ana tokha poyamba?

---

7. Ndi bwino kuchita zimenezi pamene mukufuna kuweruza ena. Kuweruza ena kumapangitsa zovuta zambiri mumpingo. Anthu amayang'ana kwa ena mmalo modziyang'ana iwo eni. Ife sitikonda zomwe ena amachita. Ife timaŵaweruza iwo. Nthawi zambiri sitidziŵa chifukwa chimene achitira zinthu zotere. Ndipo sitimamvetsetsa mavuto awo. Timadzitsekereza mwayi wokhoza kuŵathandiza iwo. Ife timaiŵala kuti ifenso tili ndi zifukwa zina.

Kuchokera pa Mateyu 7, kodi poyamba tiyenera kuchita chiyani pamene tikuganiza zofuna kuweruza ena?

---

8. Poyamba tiyenera kudziyang'ana tokha. Ngati titatero, tidzaona zifukwa zolakwa zambiri zazikuluzikulu mwa ife. Tidzaona mitanda yaikuluikulu mmaso mwathu. Pamene zimenezi zachotsedwa, timitanda ta mmaso mwa anthu ena tidzaoneka tochepa. Ife tidzakhala chifundo pamene tikulankhula za zolakwa zawo. Ife sitidzaweruza anthu ena. Tidzalankhula mwa chikondi. Ife tidzaŵathandiza kuti akhale ndi miyoyo yabwino. Kodi ife tingaone zolakwa zathu motani? Mulungu adzatithandiza. Iye amafuna kutithandiza pa vuto limeneli. Iye amafuna kutipatsanso zinthu zina zambiri zabwino.

Mateyu 7:7:

> Pemphani, ndipo chidzapatsidwa kwa inu; funani, ndipo mudzapeza; gogodani ndipo chidzatsegulidwa kwa inu.

Kodi ife tiyenera kuchita chiyani kuti tipeze thandizo kwa Mulungu?

---

9. Tiyenera kupempha. Yesu anauza ophunzira ake kuti apemphe ndi kufuna, ndikuti agogode. Anthu ena amaganiza kuti chimenechi chimatanthauza kuti upemphe munthu wina kanthu kena ndipo iye ayenera kukupatsa iwe. Koma ngati ukudzisamalira wekha suyenera kupempha ena. Ndime imeneyi ikunena za kupempha Mulungu.

Mateyu 7:8:

> Pakuti yense wakupempha alandira; ndi wakufunayo apeza; ndi kwa wogogodayo chitsegulidwa.

Kuchokera m'ndime imeneyi, kodi chimachitika n'chiyani pamene tikupempha?

---

10. Pamene ife tipempha, timalandira, ndipo pamene tikufuna timapeza. Ameneŵa ndi malonjezano odabwitsa! Amatipatsa chiyembekezo. Pamene ife tiyanjana ndi chiphunzitso chonse cha Yesu cha pa phiri, tikhoza mwina kugwetsedwa mphwayi. Tikhoza kuganiza kuti sitiyenera kutsatira Iye. Ife mwina tikhoza kuganiza kuti njira ya Chikhristu ndi yovuta ndi yolimba. Koma ife tiri ndi wina wake amene angatithandize. Iye ndi Atate wathu.

Mateyu 7:9.10:

> Kapena munthu ndani wa inu, amene pompempha mwana wake mkate, adzampatsa iye mwala? Kapena pompempha nsomba, adzampatsa iye njoka kodi?

Kodi ife timapatsa ana athu zinthu zabwino kapena zinthu zoipa?

---

11. Ife timapatsa ana athu zinthu zomwe siziri zabwino. Ife timadziŵa kuti sizingathandize ana athu. Ife sitifuna kuti ana athu azidya zinthu zowaononga. Koma pamene iwo apempha zinthu zabwino timaŵapatsa.

Mateyu 7:11:

Chomwecho, ngati inu, muli oipa, mudziŵa kupatsa ana anu mphatso zabwino, kopambana kotani nanga Atate wanu wa kumwamba adzapatsa zinthu zabwino kwa iwo akumpempha Iye?

Kodi ndi ndani amapereka zinthu zabwino m'njira yomwe ife timaperekera zinthu zabwino kwa ana athu?

______________________________

____________________________________________________________

================================================================

12. Atate athu amachita zimenezi chifukwa Iye ndi Mulungu. Iye amadziŵa zomwe ziri zabwino kwa ife. Nthaŵi zina timapempha zinthu zimene siziri zabwino kwa ife. Mulungu amayembekeza kufikira titapempha zinthu zabwino. Hana m'Buku Lopatulika anapempha mwana. Mulungu anadikira sanamuyankhe msanga kufikira anapempha kuti mwanayo adzamuperekanso kwa Mulungu.

Ayo anali kudwala. Iye anapempha kuti Mulungu amuchize. Mulungu anadziŵa kuti Ayo anafunika kuphunzira chofatso. Iye anaphunzira kusamalira zambiri za zosoŵa za ena. Iye anayembekeza kumchiritsa kufikira ataphunzira zinthu zimenezi.

Kodi ndi kwa yani kumene ife makolo timapereka zinthu zabwino monga mmene Mulungu amatipatsira ife zinthu zabwino?

______________________________

____________________________________________________________

================================================================

13. Ife timapereka zinthu zabwino kwa ana athu. Ife timaŵapatsa chakudya ndi zovala. Sitimaŵapatsa zonse zimene ali kufuna. Ife timaŵapatsa chomwe chili chabwino kwa iwo. Mulungu amafuna kuchita chimodzimodzi kwa ife.

M'njira imodzimodzi yomweyo imene timapereka zinthu zabwino kwa ana athu kodi Mateyu amanena kuti Mulungu adzatipatsa chiyani pamene ife timpempha?

____________________________________________________________

================================================================

4. Limanena kuti adzatipatsa ife zinthu zabwino. Chimenechi chimatanthauza zinthu zambiri zosiyanasiyana. Ife tikhoza kupempha Mulungu kuti atipatse chakudya, zovala ndi ndalama. Ife tikhoza kupempha ntchito yomugwirira Iye. Tikhoza kupempha thandizo la miyoyo yathu ya uzimu. Iye adzatithandiza ife pamene tikufuna kuthandiza ena powaweruza iwo.

Pamene ife tiganiza zoweruza ena, tiyenera kupempha thandizo la Mulungu, nanga kodi ife tiyenera kuchita chiyani poyamba?

======================================================================

15. Tiyenera kudziyang'ana tokha. Mulungu adzatithandiza kuti tidziyang'ane tokha. Iye adzatithandiza ife kuti tisinthe. Chimenechi ndi chinthu chimodzi cha zinthu zabwino chimene amafuna kutipatsa. Ife tikhoza kukhala Akhristu abwino. Tikhoza kukhala m'njira yomwe Yesu anaphunzitsira pa ulaliki wa pa phiri.

M'njira yomwe ife timapereka zinthu zabwino kwa ana athu, kodi Mateyu 7: amati Mulungu adzatipatsa chiyani pamene ife timupempha?

======================================================================

16. Iye adzatipatsa ife zinthu zabwino. Zinthu zimenezi zimachokera kwa Mzimu Woyera amene Mulungu amatipatsa ife. Mzimu Woyera amakhala mwa ife. Iye adzatitsogolera ngati titamulola Iye. Iye adzatipatsa mphamvu ndi chimwemwe ndi chikondi. Pa nthaŵi ina Yesu anapereka chiphunzitso chake mwa njira iyi:

Luka 11:13:

> Potero, ngati inu okhala oipa, mudziŵa kupatsa ana anu mphatso zabwino, koposa kotani nanga Atate wanu wa kumwamba adzapatsa Mzimu Woyera kwa iwo akukhulupirira Iye?

Mzimu Woyera ndi amene kupyolera mwa Iye zinthu zonse zabwino zimabwera. Kodi inu mumalola Mzimu Woyera kuti alamulire moyo wanu?

======================================================================

17. Tidzakambirana za izi tonse.

Kuchokera pa Mateyu 7, kodi poyamba tiyenera kuchita chiyani pamene tikuganiza zofuna kuweruza ena? ______________________________

______________________________________________________________

Mwa njira yomwe timapatsira ana athu zinthu zabwino, kodi Mateyu 7, amati Mulungu adzatipatsa chiyani pamene timpempha? ____________________

______________________________________________________________

==========================================================

SABATA LACHISANU NDI CHITATU: KHRISTU APHUNZITSA ZINA ZAMBIRI PA PHIRI
TSIKU LACHITATU: IFE TIYENERA KUCHENJERA NDI ANENERI ONYENGA

1. Mwina inu muli kudabwa kuti Yesu anaphunzitsa zambiri pa ulaliki umodzi. Umenewu uyenera kukhala ulaliki wautali. Kapena panali maulaliki ambiri pa phiri limenelo. Ndipo Mateyu anangoŵaphatikiza kukhala ulaliki umodzi.

Kuchokera pa Mateyu 7, kodi poyamba tiyenera kuchita chiyani tikamaganizira zoweruza ena?

______________________________

________________________________________________

Monga mmene ife timaperekera zinthu zabwino kwa ana athu, kodi Mateyu 7 amanena kuti Mulungu adzatipatsa chiyani tikamupempha?

________________________________________________

============================================================

2. Pamene tikuganiza zoweruza ena, tiyenera poyamba kudziyang'ana tokha. Pamene tikupereka zinthu zabwino kwa ana athu, moteronso Mulungu amatipatsa ife zinthu zabwino. Njira imodzi imene amatipatsa ife ndi yokhala bwino ndi ena. Pa Mateyu 7, Yesu amatiuza ife mmene tingamachitire ndi anthu ena. Iye amatiuzanso mmene tingapezere aneneri onyenga.

(1) Ife tikhoza kuganizira mmene tingachitire ndi ena poganizira mmene ife tikufunira kuti ena atichitire.

(2) Yesu ananena kuti ife tikhoza kudziŵa aneneri onyenga ndi zipatso zawo.

Tsopano tengani Buku Lopatulika ndi kuwerenga Mateyu 7:12 kufikira 23. Werenganinso ndime 12. Ngati ife titamachitira ena monga momwe tifuna akadachitira ife, kodi timamvera yani poonjezera aneneri?

________________________________________________

============================================================

3. Ife timamvera lamulo. Mulungu anapereka lamulo kwa Mose. Lamulo linali labwino. Koma Afarisi sanagwiritse ntchito bwino lamulolo m'nji-

ra yabwino. Iwo analikhotetsa kuti liŵakondweretse. Iwo anamvera mawu ndi makalata a lamulo. Koma sanamvere mtima wake wa lamulo. Yesu anati tiyenera kumvera mtima wake wa lamulo. Iye anatcha Afarisi onyenga.

Mateyu 23:23:

> Tsoka inu, alembi ndi Afarisi onyenga! chifukwa mupereka limodzi la magawo khumi la timbewu tonunkhira, ndi tsabola, ndi chotoŵe, nimusiya zolemera za chilamulo ndizo kuweruza kolungama, ndi kuchitira chifundo ndi chikhulupiriro.

Kodi ife tikhoza kumachitira anthu ena moipa ndi kumamvera lamulo la Khristu?

________________________________________

========================================================================

4. Ife sitingathe kuchita zimenezi ndi kumatsatabe njira ya Khristu. Njira imene ife timachitira ena ndi yofunika koposa. Yesu anati zifukwa zoyenera zazikulu za lamulo ndizo chilungamo, chifundo ndi chikhulupiriro. Chilungamo ndi chifundo zimalankhula zomwe timachitira anthu ena. Ife sitingachitire ena zoipa ndi kumamverabe Mulungu. Ife tiyenera kuganiza mmene ife tingafunire kuti ena atichitire ifeyo.

Mateyu 7:12:

> Chifukwa chake zinthu zilizonse mukafuna kuti anthu achitire inu, inunso muwachitire iwo zotero.

Kodi ife tiyenera kuchitira yani monga momwe tikadafuna kuchitiridwa?

________________________________________________________

========================================================================

5. Tiyenera kuchitira ena m'njira imeneyi. Chinthu chimenechi sichovuta. Ife ndife odzikonda. Timafuna zinthu zonse zabwino zikhale zathu. Timafuna kuti moyo wathu uzikhala wosavutika. Nthaŵi zina sitimafunira ena zinthu zimenezi. Sitiŵathandiza anthu kuti apeze zinthu. Taonaninso pa ndimeyi.

Mateyu 7:12:

> Chifukwa chake zinthu zirizonse mukafuna kuti anthu achitire inu, inunso muwachitire iwo zotero.

Kuchokera pa ndime imeneyi, kodi ife tikhoza kuganiza chiyani za zinthu zimene zingatithandize pofuna kuganizira kuthandiza ena?

6. Ife tikhoza kuganiza za mmene ife tikufunira kuti anthu ena azitichitira. Ine ndimafuna kuti anthu ena azindichitira chifundo. Ndimafuna kuti iwo azindikonda. Ndimafuna kuti azindikhululukira ndikalakwa. Ndimafuna kuti iwo azindithandiza pamene ndili m'mavuto.

Tsiku lina munthu wina anafunsa Yesu kuti lamulo lalikulu ndi liti.

Mateyu 22:37-39:

> Ndipo Yesu anati kwa iye, "Uzikonda Ambuye Mulungu wako ndi mtima wako wonse, ndi nzeru zako zonse, ili ndilo lamulo lalikulu ndi loyamba. Ndipo lachiŵiri lolingana nalo ndi ili, Uzikonda mnzako monga udzikonda iwe mwini."

Kodi Yesu anati uzikonda mnzako monga yani? ______________________

______________________________________________________________

==============================================================

7. Muyenera kukonda mnzanu monga inu eni. Inu simuyenera kudzida nokha ayi. Muyenera kudzisamalira bwino nokha. Mulungu amakukondani ndipo muyeneranso kudzikonda nokha. Muyenera kukonda ena.

Kodi ndi njira yotani imene ife tingaganizire yochitira ena?

______________________________________________________________

==============================================================

8. Ife tiyenera kuganiza momwe ife tikufuna kuti anthu ena azitichitira Ndipo tizichitira ena m'njira yomweyo nthaŵi zonse. M'njira imene inu mumafuna anthu kukhala achifundo kwa inu, inunso khalani achifundo kwa iwo. Inu mumafuna anthu ena kuti azikuthandizani, inunso muyenera kuthandiza. Ngati mufuna kuti anthu azikukhululukirani, inunso muziŵakhululukira.

Yesu sananene kuti njira imeneyi idzakhala yapafupi nthaŵi zonse. Iye anati nthaŵi zina ikhoza kukhala yovuta. Aneneri onyenga nthaŵi zina adzayesa kutinyenga ife.

Mateyu 7:13-14:

> Loŵani pa chipata chopapatiza chifukwa chipata chiri chachikulu, ndi njira yakumuka nayo kukuonongeka ili yotakata; ndipo ali ambiri amene aloŵa pa icho. Pakuti chipata chiri chopapatiza, ndi ichepetsa njirayo yakumuka nayo kumoyo, ndimo akuchepeza chimenecho ali owerengeka.

Kodi inu nthaŵi zina mumakhala osatsimikiza m'moyo mwanu za njira imene mungatenge?

______________________________

==========================================================================

9. Nthaŵi zina ife sititsimikiza njira yochitira zinthu. Anthu ambiri amayesa kutionetsa ife. Alaliki ambiri amayesa kutionetsa mmene tingapembedzere Mulungu. Ena a iwo ndi Akhristu oona, koma ena ayi. Yesu anadziŵa kuti chimenechi chidzaoneka. Iye anauza ophunzira za chimenechi.

Mateyu 7:15:

> Yang'anirani mupewe aneneri onyenga, amene adza kwa inu ndi zovala zankhosa, koma mkati mwawo ali afisi olusa.

Taganizirani ndime imeneyi. Nkhosa ndi zofatsa ndi zofunika kwambiri. Nyama zakuthengo zikhoza kupha. Kodi aneneri onyenga amaoneka monga chiyani?

______________________________

==========================================================================

10. Iwo amayesa kufuna kuoneka ngati nkhosa. Amayesa kuoneka abwino. Aneneri onyenga amaoneka ngati anthu abwino kunja. Koma mkati ndi anthu oipa chifukwa amafuna kutiononga.

Mateyu 7:16:

> Mudzaŵazindikira ndi zipatso zawo. Kodi achera mphesa pa minga, kapena nkhuyu pamtula?

Kodi ndi ayani tingawazindikire ndi zipatso zawo?

______________________________

==========================================================================

11. Tidzaŵazindikira aneneri onyenga ndi zipatso zawo. Zipatsozo ndi ntchito zimene amachita m'miyoyo yawo. Zipatso ndi njira za makhalidwe amene amaonekera kwa anthu ena. Mtengo wa minga ukhoza kumaoneka wobiriŵira ndi wamphamvu, koma subereka zipatso zabwino. Mneneri onyenga akhoza kumaoneka wabwino, koma iye sakhala ndi moyo wabwino.

Mateyu 7:17:
> Chomwecho mtengo wabwino uliwonse upatsa zipatso zokoma; koma mtengo wa mphuchi upatsa zipatso zoipa.

Kodi ndi Mneneri wotani amene angakhale ndi zipatso zoipa?

__________

==========================================================================

12. Mneneri onyenga adzakhala ndi zipatso zoipa. Mneneri wotere akhoza kuoneka ngati wabwino poyamba. Koma ife tikhoza kuona kuchokera ku moyo wake kuti iye siwoonadi. Iye siwotsatira wake wa Mulungu. Potsiriza Mulungu adzalanga mneneri wotere.

Mateyu 7:19-20:
> Mtengo uliwonse wosapatsa chipatso chokoma, audula, nautaya kumoto. Inde chomwecho pa zipatso zawo mudzawazindikira iwo.

Kodi inu muli kuganiza kuti ndi zinthu zotani zimene ziri zipatso zoipa m'moyo wa mneneri wonyenga?

____________________________________________

==========================================================================

13. Tidzakambirana za izi tonse pamodzi. Zipatso zoipa ndi zinthu zoipa zomwe amachita. Iye mwina akhoza kumalalikira bwino kwambiri. Koma sagwira bwino ntchito ndi ena. Iye sakonda ena. Amanyenga anthu. Mwina mwake iye sasamalira banja lake. Mwina salemekeza Mulungu. Mwina iye samvera mawu onse a Mulungu. Mwina akhoza kukonda akazi ena. Iye akhoza kumakonda zinthu za dziko lapansi. Iye amabisira anthu moyo wake ndi makhalidwe ake. Iye sakhala ndi khalidwe loonekera kuti anthu amuzindikire moyo wake.

Mateyu 7:23:
> Ndipo pamenepo ndidzafukulira iwo, "Sindikudziŵani inu nthaŵi zonse; chokani kwa Ine, inu akuchita kusaweruzika.

Kodi tingaŵadziŵe bwanji aneneri onyenga?

______________________________

____________________________________________________________

===================================================================

14. Ife tikhoza kudziŵa aneneri onyenga ndi zipatso zawo. Yesu anati siyense amene amamutchula kuti "Ambuye" adzaloŵa ufumu wa kukwamba. Mneneri woonadi amachita zomwe Mulungu amanena. Ife masiku ano tili ndi aneneri onyenga mmalo otizungulira. Anthu amalalikira zinthu zosiyana zambiri. Ngati mneneri ali wonyenga, ife sitingakhulupirire mawu ake. Ife tidzamuzindikira ndi zipatso za moyo wake. Chipatso china choipa ndi kulephera kukhala bwino ndi anthu. Chimenechi chili kutikumbutsa ife gawo loyamba la phunziroli.

Kuchokera pa chiphunzitso cha Yesu cha pa phiri, kodi ndi njira yotani imene ife tiyenera kuganizira zochitira anthu ena?

______________________________

____________________________________________________________

===================================================================

15. Timachita zimenezi pamene tikuganizira za anthu ena mmene azichitira kwa ife. Tiyenera kumakonda ena monga momwe ife timadzikondera. Timayenera kukhala ndi mphatso zabwino m'miyoyo yathu.

Mateyu 7:21:

> Siyense wakunena kwa Ine "Ambuye, Ambuye, adzaloŵa mu Ufumu wa Kumwamba; koma wakuchitayo chifuniro cha Atate wanga wa Kumwamba.

Kodi Yesu anati tikhoza kudziŵa aneneri onyenga motani?

____________________________________________________________

===================================================================

16. Tikhoza kuŵadziŵa iwo ndi zipatso zawo. Sule ali ndi vuto. Iye wakhala ali Mkhristu kwa zaka zitatu. Masabata apitawo munthu anafika kunyumba kwake. Iye anamfunsa Sule kuti atsatire Mulungu m'njira yatsopano anamuuza kuti sitiyenera kupembedza Mulungu mnyumba. Iye anati, sitiyenera kupembedza monga momwe mpingo umaphunzitsira. Iye anamuuza

Sule zinthu zatsopano zambiri. Iye anati pali malamulo ena ambiri atsopano amene timayenera kuŵatsata. Iye anatsutsana ndi Sule za Buku Lopatulika. Iye ananena kuti mlaliki wa Sule simunthu wabwino. Ndipo Sule anasokonezeka.

Kuchokera mphunziro lalero, kodi mudakamuuza chiyani Sule ngati mukadalankhulana naye?

________________________________________

____________________________________________________

===========================================================================

17. Tidzakambirana tonse pamodzi za vuto la Sule.

Kuchokera m'chiphunzitso cha Yesu cha pa phiri, kodi ndi m'njira zotani zimene ife tiyenera kuganizira pochitira ena zinthu?

________________

____________________________________________________

Kodi Yesu anati tikhoza kuŵadziŵa motani aneneri onyenga?

____________________________________________________

===========================================================================

SABATA LACHISANU NDI CHITATU: KHRISTU APHUNZITSA ZINA ZAMBIRI PA PHIRI
TSIKU LACHINAYI: KUMVERA KHRISTU KULI MONGA KUMANGA NYUMBA PA THANTHWE

1. Ili ndi phunziro lotsiriza la chiphunzitso cha pa phiri. Pali zinthu zina zambiri zoyenera kuphunzira kuchokera m'mawu a Yesu. Pamene muli ndi nthaŵi, phunzirani Mateyu 5;6; ndi 7. Mudzapeza chakudya chanu china chambiri. Mudzapezanso maulaliki ena abwino ambiri oyenera kuŵalalikira.

Kuchokera pa chiphunzitso cha Yesu cha pa phiri, kodi ndi njira yotani imene ife tingaganizire zochitira ena zinthu? ______________________

________________________________________________

Kodi Yesu anati ife tikhoza kudziŵa aneneri onyenga motani?

________________________________________________

================================================

2. Mmene ife tifunira kuti ena azichitira ndi mmenenso tiyenera kuchitira ena. Ife tikhoza kudziŵa aneneri onyenga ndi zipatso zawo.

Yesu anatsiriza chiphunzitso chake cha pa phiri ponena nthano. Nthanoyo ndi ya anthu aŵiri. Munthu mmodzi anamanga nyumba yake pamalo ofeŵa. Nyumba yake siinakhale nthaŵi yaitali. Chimenechi ndi chimene Yesu anafuna kuphunzitsa:

(1) Munthu amene anamanga pa nthanthwe afanana ndi amene amamvera mawu Khristu.
(2) Munthu amene anamanga pa mchenga afanana ndi munthu wosamvera.

Tsopano tengani Buku Lopatulika ndi kuwerenga Mateyu 7:24 mpaka 29. Kodi aliyense amene amamva mawu a Yesu amamvera zomwe Iye amanena?

______________________

================================================

3. Anthu ambiri sachita. Anthu ambiri amamva Yesu pamene anali pa dziko lapansi. Koma ambiri a iwo samvera mawu ake. Yesu anakwiya za zimenezi. Iye anadziŵa kuti ndi zosakwanira kuti anthu angomva kokha za Iye.

Iye anali kulankhula ndi anthu tsiku ndi tsiku. Ena mwa iwo anamumvera Iye akulankhula tsiku ndi tsiku. Iwo adzadziŵa bwino chiphunzitso chimenechi. Koma sanamvere. Iye anadziŵa kuti iwo si anthu anzeru.

Mateyu 7:24:
Chifukwa chimenechi yense amene akamva mawu anga ameneŵa ndi kuŵachita, ndidzafanizira iye ndi munthu wochenjera, amene anamanga nyumba yake pathanthwe.

Kodi munthu wochenjera anamanga nyumba yake kuti?

______________________

==========================================================================

4. Iye anaimanga pa thanthwe. Iye anafuna kumanga nyumba ya mphamvu. Iye anafuna nyumba yomwe ikadakhala nthaŵi. Mwina iye anali kumanga nyumba ya njerwa. Nyumba yolimba iyenera kukhala ndi maziko. Iyenera kukhala ndi pena pake pamene ingakhazikike kuti isasunthike.

Mkhristunso amafunika kanthu kena kolimba komwe angaimirirepo. Iye sayenera kumanga nyumba yamoyo wake pa kanthu komwe kamasintha nthaŵi zonse. Yesu anati mawu ake adzakhalabe ku nthaŵi zonse.

Mateyu 24:35:
Thambo ndi dziko lapansi zidzachoka, koma mawu anga sadzatha.

Komatu sikukwanira kungomva mawu a Yesu. Pamene ife timva mawuwo, kodi tiyenera kuchita chiyani ndi mawuwo?

____________________________________

__________________________________________________________________________

==========================================================================

5. Ife tiyenera kuwamvera mawu ake. Tiyenera kutsata chiphunzitso chake. Ife tiyenera kumamanga miyoyo yathu tsiku tsiku pa zimene Yesu amanena. Munthu wochenjera anamanga nyumba yake pa thanthawe. Anthu ambiri anadza kwa Iye. Iye anali ndi mayesero ambiri. Koma moyo wake sunagwe.

Mateyu 7:25:
Ndipo inagwa mvula, nidzala mitsinje, ndipo zinaomba mphepo zinagunda pa nyumbayo, koma siinagwe; chifukwa inakhazikika pa thanthwepo.

Kodi anthu amene amamva mawu a Yesu ndi kuŵamvera mawuwo ali ofanana ndi chiyani?

6. Iwo afanana ndi munthu amene anamanga nyumba pa thanthwe. Yesu anadziŵa kuti mavuto ndi mayesero ambiri zidzafika kwa anthu ake. Ife tidzayesedwa. Tidzakhala tili kulondedwalondedwa. Ife tidzakhala tili kuvutidwa ndi aneneri onyenga. Koma ngati ife tili Akhristu anzeru sitidzabwerera m'mbuyo. Miyoyo yathu siidzagwa. Sitidzasiya kukhala Akhristu.

Kodi Yesu anati ndi ndani amene ali wofanana ndi munthu wochenjera amene anamanga nyumba yake pa thanthwe?

7. Munthu wanzeru ndi amene amamvera mawu a Yesu. Koma ambiri sanamvere. Iwo anati mawu ake ndi ovuta kwambiri. Iwo ankanena kuti akufuna kudyerera moyo wawo. Ena amayerekeza kukhala Akhristu. Iwo amayesetsa kumanga okha miyoyo yawo kuti azioneka ngati abwino.

Mateyu 7:26:

> Ndipo inagwa mvula, niidzala mitsinje, ndipo zinaomba mphepo, zinagunda pa nyumbayo; ndipo inagwa; ndi kugwa kwake kunali kwakukulu.

Kodi Yesu anatcha chiyani munthu amene anamanga nyumba pa mchenga?

8. Yesu anamutcha kuti ndi wopusa. Ntchito yake yonse inalibe phindu. Chimenechi ndi chimodzimodzi ndi amene amamva mawu a Khristu koma samumvera. Yesu analankhula za zimene Mulungu amafuna. Mawu ake amatiuza za choonadi cha Mulungu. Iwo amatiuza zimene Mulungu amafuna kuti tichite. Amatiuza mmene tiyenera kukhalira.

Mateyu 7:21:

> Siyense wakunena kwa Ine, Ambuye, Ambuye, adzaloŵa mu Ufumu wa kumwamba; koma wakuchitayo chifuniro cha Atate wanga wa kumwamba.

wanga wa kumwamba.

Ngati ife sitifuna kumvera mawu a Yesu, kodi tikumanga pa thanthwe kapena pa mchenga?

______________________________

==============================

9. Tikumanga pa mchenga. Ife tikuyerekeza kukhala Akhristu. Timachita zinthu zina zimene Akhristu amachita. Timayesa kumaoneka monga Akhristu Koma tili monga munthu wopusa. Ntchito yathu njopanda pake.

Mateyu 7:27:
Ndipo inagwa mvula, nidzala mitsinje, ndipo zinaomba mphepo zinagunda pa nyumbayo, ndipo inagwa; ndi kugwa kwake kunali kwakukulu.

Kodi chingaoneke ndi chiyani kwa miyoyo yathu ngati tili wopusa ndi kusamvera mawu a Khristu?

______________________________

==============================

10. Miyoyo yathu idzagwa. Tikungotaya nthaŵi yathu. Timayesa kukhala ndi miyoyo yabwino koma imakhala yofooka. Imakhala yopanda pena poimirirapo. Iyo siingakhale yolimba pamene mavuto ndi mayesero angabwere. Iyo idzasweka pamene idzakumana ndi mayesero amkuntho wa moyo.

Kodi ndi mawu ayani amene ife tiyenera kumamvera ngati sitifuna kumanga miyoyo yathu pa mchenga?

______________________________

==============================

11. Ife tiyenera kumvera mawu a Yesu.

Kodi ndi munthu wotani amene anamanga nyumba yake pa mchenga?

______________________________

==============================

12. Amene samvera afanana ndi munthu amene anamanga nyumba pa mchenga. Ife tiyenera kumvera mawu a Khristu. Ngati sitimutsata Iye, miyoyo yathu idzagwa pansi. Tidzakhala ofooka pamayesero a Satana. Pomaliza tidzafa m'machimo athu.

Mateyu 7:22-23:

> Ambiri adzati kwa Ine tsiku lomwelo, Ambuye; kodi sitinanenera mawu m'dzina lanu, ndi m'dzina lanunso kutulutsa mizimu yoipa, ndi kuchita m'dzina lanunso zamphamvu zambiri? Ndipo pamenepo ndidzawafukulira iwo, sindikudziwani inu nthaŵi zonse, chokani kwa Ine, inu akuchita kusaweruzika!

Monga tinaphunzira dzulo, kodi Yesu anati tikhoza kudziŵa aneneri onyenga motani?

________________________________________________________

==========================================================================

13. Timaŵadziŵa aneneri onyenga ndi zipatso zawo. Miyoyo yawo siibweretsa zinthu zabwino. Iwo samvera mawu a Khristu. Ife timadziŵa kuti zipatso zabwino sizitipulumutsa ife. Ife timapulumutsidwa ndi chikhulupiriro cha mwa Khristu. Koma ngati tikhulupiriradi mwa Khristu, tidzamvera mawu ake.

Kodi ndi ndani ali monga munthu wopusa yemwe anamanga nyumba yake pa mchenga?

____________________________________________________________

==========================================================================

14. Ndi amene samvera mawu a Khristu. Iye ali monga munthu wopusa amene anamanga nyumba yake pa mchenga. Yesu anaphunzitsa zinthu zambiri mu mzinda. Iye anafuna kuti anthu amvere zinthu zimenezi. Iye anafuna kuti iwo aike zinthu zabwino m'miyoyo yawo. Iye sanangofuna kuti iwo angosunga lamulo. Iye anafuna kuti iwo akhale olungama m'mitima yawo.

Kodi Yesu ananena kuti ndi munthu uti wa nzeru yemwe anamanga nyumba yake pa thanthwe?

________________________ _______________________________

_______________________________________________________________________

==========================================================================